anayankhidwira, ndi kupeza nthaŵi yakumuthokoza Mulungu.

8. Kodi Yesu anati chingachitike ndi chiyani ngati anthu aŵiri kapena kuposera apo atagwirizana kuti apempherere chinthu china chake?

________________________________________

________________________________________

==================================================

Ndi chinthu chofunika kwambiri kuti mapemphero a m'chalichi asamakhale aatali. Makamaka ndi kofunika kwambiri kuti mapemphero a m'banja azikhala achidule. Lolani aliyense kuti apemphere. Lolani mapemphero anu kuti akhale achidule ndi omveka. Pamene wina atsogolera mapemphero, lolani ena kuti azipemphera m'mitima mwawo. Gwiritsani ntchito mawu amene ali osabvuta ndi wochokera pansi pa mtima. Phunzitsani ana anu kulankhula ndi Mulungu mokhulupirika.

9. Kodi muganiza kuti mungathe kupanga mapemphero a banja kukhala abwino kwambiri pakutha pa phunziro ili?

________________________________________

10. Kodi ndi chiyani chimene banja lingachite pamodzi tsiku ndi tsiku?

________________________________________

==================================================

*************************************************************

MAYANKHO

5. Pakumvera anakubala awo akupemphera ndikuyesera okha kupemphera.
2. Kunyumba ndi makolo.
9. Ndiyembekeza mudzayesa.
6. Ndinafunsa zimene mumaganiza, choncho ndibvomera yankho lanu, koma ndiganiza kuti ichi ndi chofunika kwambiri.
4. Inde.
8. Iye anati zidzachitidwa ndi Atate ali kumwamba.
3. Chingathe kukhala chilichonse monga kusesa, kudula nkhuni, kuphika, kapena kukama mkaka.
7. Tiyenera kuti tisiye kupemphera ndi kupita kukachita chinthu chija kuti chikhale bwino.
1. Tidzalankhula bwino zimenezi m'kalasi.
10. Banja lonse liyenera kupemphera pamodzi.

ABATA LACHISANU NDI CHITATU: KUPEMPHERA NDI ANTHU ENA
TSIKU LACHISANU:

Kodi sabata lonse lathunthuli mwaphunzira zotani?

1. Lembani ubwino wakupemphera pamodzi ndi anthu ena.

______________________________

______________________________

______________________________

==========================================================

2. Lembani magulu aŵiri a anthu amene tiyenera kupemphera nawo pamodzi.

(1) ____________________ (2) ____________________

==========================================================

Palinso gulu lina limene lili labwino lofunika kwambiri kupemphera nalo. Ili ndi gulu laling'ono limene mumasonkhana nalo pamodzi ndi cholinga chofuna kupemphera. Nthaŵi zina pamapezeka zofunika zina zimene sizingathe kupempherere-redwa ndi mpingonso. Nthaŵi zina zofunikazi sizikhudza banja. Koma wina wake ayenera kutanganidwa pakupempherera zofunikazi. Ndani ayenera kuchita zimenezi? Lero tiyeni tiphunzire za magulu a ang'ono opemphera.

3. Kodi munayamba mwapemphererapo chinthu china chake kwa nthaŵi yaitali osapeza mayankho?

____________________

==========================================================

Kumbukirani kuti Yesu ananena kuti nkwabwino kwa anthu aŵiri kapena kuposera apo kukhala pamodzi nkupemphera.

Mateyu 18:19-20:

Ndiponso ndinena kwa inu kuti ngati awiri a inu abvomerezana pansi pano chinthu chilichonse akachipempha, Atate wanga wa kumwamba adzaŵachitira. Pakuti kumene kuli aŵiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndili komweko pakati pawo."

4. Kodi mungathe kunena ndime zimenezi osayang'anira m'buku? Ngati simungathe lekezani tsopano, ndipo mubwereze ndime zimenezi mpaka mutaziloweza pamtima.

==========================================================

Mwina inu mukufuna china chake chachikulu chimene muli kuchipempherera. Angathe kukhala munthu wina wake amene sali Mkhristu kuti atembenuke mtima. Kapena lingakhale tchimo limene lili mu mpingo limene lifunika kulichotsa. Kapena mwina mufuna kuona chitsitsimutso mumpingo. Mwakhala muli kupempherera zinthu zimenezi koma osapeza mayankho. Choncho iyi ndiyo nthaŵi yokaona anthu ena kuti mukhale nawo pamodzi popemphera.

5. Talembani dzina la munthu wina amene muganiza kuti angakhale nanu popemphera.

______________________________

==========================================================

Ena a inu munaphunzirapo kale za pemphero la mtundu uwu kuchokera m'maphunziro a "Moyo Watsopano kwa Onse." (New Life for All Movements). Chiphunzitso ichi chimafuna kuona umoyo watsopano mumpingo. Chimatiphunzitsa m'mene tingapitire ndi kukauza anthu ena za Khristu. Koma poyamba penipeni chimatiphunzitsa za mmene tingapempherere.

6. Kodi "Moyo Watsopano kwa Onse" umatiphunzitsa kuti tizipemphera m'modzi-m'modzi?

____________________

==========================================================

Magulu aang'ono amene amafuna kupempherera zosowa zawo mu mpingo ayenera kuyesa kumakumana tsiku ndi tsiku kapena

masiku angapo pa sabata. Iyi sinthaŵi yolalikira kapena yoimba ayi. Koma ndi nthaŵi yamapemphero. Mapemphero akenso sayenera kukhala ataliatali. Munthu aliyense ayenera kupempherera chinthu chimodzi pa nthaŵi imodzi. Ngati mapemphero akhala achidule kumakhala kosabvuta kuti anthu ena atsatire zonenedwazo, ndipo munthu aliyense akhoza kupemphera kaŵiri kapena katatu. Kuteroku kuli ngati kukambirana nkhani. Inu nonse mwakhaladi pamodzi ndi kumalankhula ndi Mulungu.

7. Kodi munayamba mwayeserapo kupemphera kwa mtundu umenewu?

____________________

==========================================================

Koma mwina mwake simudziŵa munthu aliyense amene angafune kuloŵa nawo m'gulu lopemphera laling'onoli. Simudziŵanso kayambidwe kake. Nanga mukhoza kuchita chiyani? Choyamba muyambe kupempha Mulungu kuti akupatseni wina wake kuti mupemphere naye pamodzi. Mumuuze kuti ananena kuti aŵiri kapena atatu azisonkhana kuti azipemphera. Mumuuze kuti inu mufuna kuchita zimenezi. Mumupemphe kuti akupezereni bwenzi amene amafuna kupemphera.

8. Kodi Mulungu adzayankha pemphero lanu mwamsanga?

____________________

==========================================================

Ngati inu mufunitsitsadi kupemphera ndi munthu wina kapena ndi kagulu kakang'ono ndiye kuti Mulungu adzakutsekulirani njira. Ngati mnzanu kapena anzanu amakhala kutali kwakuti simungathe kumakomana nawo tsiku ndi tsiku, ndiye kuti muyenera kumakomana kamodzi kapena kaŵiri pa sabata koma mugwirizane kupempherera zosoŵa zanu tsiku lililonse. Mwa njira imeneyi mudzakhala muli kupemphera pamodzi ndi anthu ena ngakhale mutapanda kukhalira pamodzi.

9. Kodi muli wokondweretsedwa kuyesa kupemphera kwa mtundu umenewu?

Ngakhale mwamuna ndi mkazi wake akhoza kupanga kagulu kakang'ono kopemphera. Iwo akhoza kumakumana kwa nthaŵi yochepa tsiku lililonse kungopempherera zofuna zawo zimene iwo agwirizana. Kupemphera pamodzi kwa mtundu uwu kudzalimbikitsa chikhulupiriro chawo ndipo mapemphero awo adzayankhidwa.

10. Mosaonera m'Buku Lopatulika, lembani Mateyu 18:19-20.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

==========================================================

11. Kodi njira yabwino yopempherera zosowa zapadera ndi yotani?

______________________________________

______________________________________________

***********************************************************

MAYANKHO

1. Mulungu alipo. Mulungu analonjeza kuti adzayankha mapemphero ogwirizana.
3. Muyenera kuyankha zimenezi.
5. Muyenera kusankha wina.
9. Izi zili kwa inu.
7. Izi zili kwa inu.
11. Yambani magulu aang'ono a màpemphero.
2. (1) Akhristu (2) Banja.
4. Muyenera kuchita zimenezi.
6. Ayi.
8. Kapena, koma nthaŵi zina zimatenga nthaŵi.
10. Pezani ndime imeneyi m'Buku Lopautlika ndipo muone yankho lanu ngati lili lokhoza.

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: MAYANKHO A MAPEMPHERO
TSIKU LOYAMBA:

Tsopano taphunzira magawo a mapemphero osiyanasiyana. Koma timadziŵa kuti kuphunzira zimenezi m'mutu mwanu kuli kosiyana kwambiri ndi kumazigwiritsa ntchito pa moyo wanu. Mungathe kufotokoza zilizonse za mapemphero, koma osapemphera mokhulupirika. Mungathe kudziŵa za malonjezo a Mulungu, koma osaŵagwiritsa ntchito kuti mapemphero anu ayankhidwe.

Sabata ino tikufuna kuyesa kukuthandizani kuti mupange pemphero kuti likhale mbali ya moyo wanu. Sipadzakhalanso mafunso m'maphunziro ameneŵa. M'malo mwake ife monga olemba bukuli, tikufuna kukuuzani mmene pemphero limagwirira ntchito m'miyoyo mwathu ndi m'miyoyo mwa anthu ena amene tamvera. Mudzakhala muli kuwerenga limodzi la yankho mwa mayankho a pemphero tsiku lililonse. Ndipo kenaka tidzakupemphani kuti mupempherere chinthu china chake pa tsikulo. Iyi ndiyo ntchito yanu ya sabata ino.

Kungakhale kobvuta kuti inu mumvetsetse nditakuuzani kuti mmodzi mwa anthu olemba buku ili anali mbiyang'ambe, chidakwa kapena kuti chigona m'bawa, ndipo iye anali kuti akamwa mowa choncho anali kugona nawo m'misewu osazindikira njira yakunyumba kwake.

Ine, Fred Holland, atsibweni anga ankanditenga kupita nane kukamwa moŵa ndisanakwane zaka zisanu ndi chimodzi zobadwa. Nditafika zaka khumi ndi zitatu ndinathaŵa sukulu. Ndinapalana ubwenzi ndi anyamata ena okulirapo, amene anali kumwa moŵa ndi kuba. Mmene ndinakula ndinagwira ntchito zambiri.

Ndinapitirizabe kumwa moŵa ndi kuyesa kupeza moyo wachinyamata wokondweretsa. Mnyamata wina ndi ine tinali kuba magalimoto ndi kuchotsa matayala ndi zipangizo zina za galimotoyo ndi kugulitsa. Ndipo kaŵirikaŵiri ndinali kukhala m'ndende. Tsiku lina ndinali kuchipatala kudwala chifukwa chopezeka kuti ndinamwa moŵa kwambiri, koma ndinathaŵako. Nthaŵi zonsezi mkulu wanga anali kuyesetsa kundithandiza. Mkulu wangayu analidi Mkhristu woona mwakuti anali kulalikira m'tchalitchi china chake chaching'ono. Nthaŵi zina ndinali kubwera kunyumba kwa mkulu wanga nditaledzera, koma iye

anali kundidambitsa nandigoneka pamalo ogona.

Kenaka ndinalowa usilikali wa nkhondo. Kumeneko ndinali ndi ntchiti ziŵiri. Ntchito yoyamba inali yophunzitsa asilikali anzanga kuomba mfuti, ndipo ina inali yoperekera maŵa ku bawa. Nthaŵi zina anzanga anali kunditengera kunyumba kuchokera ku bawako ndi kukandigoneka chifukwa sindinali kuona njira chifukwa choledzera kwambiri.

Tsiku lina ndinaswa sitolo ndikubamo zinthu zambiri za mtengo wapatali. Kenaka ndinaikidwa m'ndende yaikulu kwa masiku angapo. Potsirizira pa mwezi wa October, 1948, nthaŵi anga yakuti ndisiye ntchito kunkhondo inakwana. Ndinali kumwa kwambiri, koma mkulu wanga ndi anthu ena ampingo anali kundipempherera nthaŵi zonse ku tchalitchi. Kenaka ndinaona kuti ndinayamba kuona momwe ulili moyo wanga pamaso pa Mulungu. Anthu ampingo anamva kuti ndinali kubwera kumudzi. Iwo anapemphera m'njira ina yake yapadera.

Pa tsiku loyamba la sabata usiku, nditangobwera kumudzi misonkhano yapadera inayambika m'tchalitchi. Ndinapita ku msonkhano wa chitsitsimutso ku tchalitchi. Pa msonkhano umenewu mtima wanga unabvutika kwambiri. Msonkhano uli mkati ndinatuluka pabwalo ndi kung'amba ka paketi ka fodya wa ndudu kamene ndinali nako m'thumba. Pakutha pa msonkhano umenewu, ndinapita kutsogolo kukapemphera. Ndinalira pamene Mulungu anandisonyeza machimo anga onse amene ndinali kuchita pa moyo wanga wonse. Kenaka ndinamulandira Khristu kukhala Mpulumutsi wanga ndipo ine ndekha ndinadziŵa kuti mtima wanga unasinthidwa. Kuchokera pa tsiku limenelo mpaka lero sindinamwenso moŵa. M'malo mwake ndinapita ku maphunziro a Buku Lopatulika, (Bible School), kenaka ayi ndithu ndinakhala wamishoni.

Zonsezi zinachitika chifukwa mkulu wanga ndi mpingo anali kundipempherera.

Mukamaganiza kuyankhidwa kwa pemphero ili, kumbukirani wina wake m'banja lanu amene afunika kuti atembenuke mtima ndi kusiya zoipa zake zonse. Imani ndipo mumpempherere iye pakali pano. Mpempheni Mulungu kuti amusonyeze tchimo lake. Mpempheni Mulungu amusonyeze mmene Yesu anamufera pamtanda kumumasula ku machimo ake. Mpemphani Mulungu kuti akuthandizeni kuti mupitirize kumupempherera amene ali m'banja

mwanu kuti akhalenso Mkhristu.

2 Akorinto 5:17:

Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano, zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano.

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: MAYANKHO A MAPEMPHERO
TSIKU LACHIŴIRI:

Yankho lachiŵiri la mapemphero limachokera ku Nigeria, Africa. Mungathe kuwerenga nthano yonse kuchokera ku buku lotchedwa "New Life for All" lolembedwa ndi Eileen Lageer, (Moyo Watsopano kwa Onse, wolemba Eileen Lageer).

Pamene chiphunzitso cha Moyo Watsopano kwa Onse chinaperekedwa kwa anthu aku Nigeria, kumeneko kunali munthu wa zaka zambiri yemwe dzina lake ndi Makafo. Ameneyu anali kufuna kuthandiza ntchitoyo. Koma iyeyo anali nkhalamba, wosaona, ndipo sanali kutha kuyenda kupita kukalalikira, koma anali kupemphera. Iye anaganiza kupempha atsogoleri amene anali kulalikira kuti ampatse maina a anthu amene sanali kufuna kumva Uthengawo. Iye analonjeza kuti aŵapempherera m'njira yake yapadera.

Atsogoleri anabvomereza kuti adzamupatsa mainawo. Potsiriza anabwera ndi maina khumi ndi limodzi kwa iye. Aŵa ndiwo anali anthu obvuta m'miyoyo mwawo ndipo anali kuoneka ngati kuti sangathe kutembenuka mtima.

Bambo Makafo anaŵapemphera anthu ameneŵa mokhulupirika tsiku lililonse akamakhala wokha kunyumba kwawo, pokhala iwo anali wokalamba ndiponso wosatha kuona kapena kuyenda. Iwo anawapempherera onse m'modzi monga mwa maina awo.

Miyezi inalikutha. Bambo Makafo anali kukhumudwa nthaŵi zina, koma iwo anapitirizabe kupemphera. Ndipo mapemphero aja anayamba kuyankhidwa. Kodi mungathe kuganiza mmene iwo anamvera pamene anaona munthu amene anali kumpempherera uja atabwera tsiku lina kunyumba kwawo kudzaŵachezetsa? Munthuyo sanangobwera kudzangolankhula nawo kokha ayi. Koma anabwera kudzapempha Bambo Makafo kuti ampempherere ndi kuti iyenso adzipempherere yekha kuti machimo ake akhululukidwe.

Atatha uyo, panabweranso wina. Nkudzanso wina. Nkudzanso wina. Chaka chisanathe, onse aja amene anali kupempheredwa ndi Bambo Makafo anabwera kukanyumba kawo kudzapemphera ndi kudzalandira moyo watsopano mwa Khristu.

Kodi inu mukanabvomera kuti mupempherere anthu obvutitsa m'mudzi mwanu monga m'mene anachitira Bambo Makafo? Kodi mukanapemphera kokwanira chaka chonse mpaka onse atatembenuka mitima? Uwu ndiwo mtundu wa mapemphero umene Mulungu amayankha.

Mukamaganizira za yankho ili kumbukirani za wina wake m'mudzi mwanu amene akukana kumva ulaliki wonena za Yesu Khristu. Mwina mwake munthu ameneyu ndi wobvuta kwambiri. Iye amaoneka ngati kuti sangathe kutembenuka mtima. Kapena chikhulupiriro chanu chimachepa mukamaganizira zimenezi, koma kumbukirani kuti chikhulupiriro chaching'ono monga kambewu, chikhoza kupanga zodabwitsa.

Tayambani mwaima ndipo mupempherere Bambo kapena Mayi wobvutayu amene ali m'mudzi mwanu ndipo mumpemphe Mulungu kuti akuthandizeni kuti mupitirizebe kumpempherera mpaka munthu ameneyu atatembenuka mtima.

Mateyu 17:20b:

> Pakuti indetu ndinena kwa inu, mukakhala nacho chikhulupiriro monga kambewu ka mpiru, mudzati ndi phiri ili, "Senderapo umuke kuja," ndipo lidzasendera; ndipo palibe kanthu kadzakulakani kosachitika.

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: MAYANKHO A MAPEMPHERO
TSIKU LACHITATU:

Yankho lotsatira la pemphero lili kusonyeza ubwino wake wogwirizana ndi munthu m'modzi kapena aŵiri pamene mufuna kupempha chinthu china chake. Yankho la pemphero ili linalembedwa m'buku lotchedwa, Nkhani Zakachetechete pa Mapemphero, lolembedwa ndi S.D. Gordon. (Quiet Talks on Prayer, by S.D. Gordon).

Bambo Gordon amene ali mlembi wa buku limeneli, anali ndi mnzawo amene anaŵauza mbiri ya mmene anakhalira Mkhristu. Izi ndi zimene zinachitika. Bwenzi la a Gordon anali munthu wamkulu msinkhu ndiponso anali ndi udindo waukulu pa ntchito yake. Iye anali wochenjera kwambiri ndiponso wodziŵa za malamulo (Lawyer). Pambuyo pake anasankhidwa kuti agwire ntchito ya kunyumba ya malamulo, imene inali mbali yofunika kwambiri mboma la United States.

Koma munthu ameneyu sanali Mkhristu. Iye anali kunena kuti sanali kukhulupirira kuti Mulungu alipo, ndipo anali ndi anzake enanso mboma momwemo amene anali kugwirizana naye pa zikhulupiriro zake.

Mosadziŵika bwino tsiku lina pamene munthu ameneyu anali pa msonkhano waukulu wa boma anamudzera maganizo akuti Mulungu anali naye pamalo amene analipo ndipo sanali okondwa ndi mmene iye anali kukhalira. Koma munthu ameneyu sanali kukhulupirira Mulungu ndipo mwa ichi sanali kukondweretsedwa kuti aziganiza kuti Mulungu alipo. Iye anaganiza kuti anali kugwiranso ntchito molimbika kuposera mphamvu zake, ndipo mwa ichinso sanali kuganiza bwino. Iye anangochoka nasiya msonkhano nkupita pabwalo kukapuma mwakungoyendayenda chabe.

Koma izi sizinathandize. Koma zikuonekabe ngati kuti Mulungu anali kulankhula naye ndipo iye sanali kutha kumuthaŵa Mulungu. Izi zinapitiririrabe koposa miyezi itatu mpaka ntchito ya boma pa nthaŵi imeneyo itatha ndipo anapita kumudzi kwawo kwa kanthaŵi. Pamene anafika kumudzi anapeza kuti mkazi wake ndi akazi ena aŵiri amene anali Akhristu, anagwirizana za kumpempherera kuti akhale Mkhristu. Iye anafunsa mkazi wake kuti anayamba liti kumpempherera m'njira

imeneyi. Mayi uja anamuuza, ndipo iye anadziŵa kuti ili linali tsiku limene iye anali mu msonkhano pamene Mulungu anayamba kulankhula naye.

Bambo ameneyu anali wodabwa kwambiri pamene anamva zimenezi mwakuti anayamba kubvutika mumtima mwake. Iye anati anali wosakhulupirira Mulungu ndipo anzake onse anadziŵa zimene iye anali kunena. Koma sangakane kuti Mulungu anali kugwira ntchito pakuyankha mapemphero a mkazi wake. Masiku ambiri anali kubvutika mumtima mwake ndipo tsiku lina usiku iye ananyamuka pamodzi ndi mkazi wake kupita ku tchalitchi. Pambuyo pake anatsalira alikupemphera, ndi kumlandira Khristu. Kuchokera nthaŵi imeneyo moyo wake unasinthika. Iye anaganiza zakuti asiye ntchito ya boma kuti akhale mlaliki wa Mulungu.

Pamene Bambo uja ndi mkazi wake anali kufotokozera a Gordon nkhani iyi, mkazi wa Bambo uja anati nayenso anamva mawu a Mulungu. Pamene anali kupempherera mwamuna wake usiku wina kuti apulumutsidwe, kunangomveka mawu achifatse akuti, "Kodi ulikufuna kubvomereza chilichonse chimene chidzachitike?" Poyamba sanadziŵe kuti izi zinali kutanthauza chiyani ndipo anangopitirirabe kupemphera. Koma mawu anadzanso kwa iye nati, "Kodi ulikufuna kubvomereza chimene chidzachitike? Mawu awa anali kungobwererabwererabe mpaka iye anapemphera ndi kumuuza Mulungu kuti anali kufuna chilichonse chimene chikanachitika ngati mwamuna wake akanangokhala Mkhristu.

Mwina mwake inu muli kudabwa kuti chidzachitike ndi chiyani kwa iye. Monga mkazi wa munthu wogwira ntchito m'boma, mkazi ameneyu anali ndi ndalama zambiri ndi udindo waukulu kwambiri, koma pamene mwamuna wake anangosiya ntchito yake nakhala mbusa sanakhalenso ndi mipando yonseyo m'bomamo ayi. M'malo mwake anali kungokhala ndi ndalama zochepa zokha zimene mbusa amapeza, ndipo nthaŵi zambiri anali kusamukira komwe mwamuna wake anaitanidwa kukalalikira ku malo atsopano. Koma iye anali wokondwa pa zonsezi chifukwa Mulungu anayankha mapemphero ake.

Lero mukamaganizira za mmene Mulungu anayankhira mapemphero a mayi uyu pamodzi ndi anzake aja aŵiri, sankhani m'tsogoleri wina aliyense m'mudzi mwanu kapena m'boma lanu amene sali Mkhristu. Tayambani tsopanoli kumpempherera munthu wachikulire ameneyu.

Mateyu 18:19:

Ndiponso ndinena kwa inu kuti ngati aŵiri a inu abvomerezana pansi pano, chinthu chilichonse akachipempha, Atate wanga wa kumwamba adzawachitira.

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: MAYANKHO A MAPEMPHERO
TSIKU LACHINAYI:

Ngakhale pamene tinali kulemba maphunziro amenewa Mulungu anali kuyankhabe mapemphero athu pa mishoni pamene timakhala.

Chaka chatha ophunzira apano pa Sukulu ya Maphunziro a Buku Lopatulika, (Bible School) anakachezera mayi wina pafupi ndi pa mishoni amene sanali Mkhristu, ndipo anamufotokozera za njira ya chipulumutso. Mayi ameneyo ananena kuti iye anafuna kuti atembenuke mtima, kanaka iye anapemphera pemphero la kubvomereza machimo ake nakhulupiriranso pa tsiku lomwelo pamene anakamuchezera. Kuchokera pa nthaŵi imeneyo aphunzitsi ndi ophunzira a Maphunziro a Buku Lopatulika (Bible School) anapemphera kuti mayi ameneyo aziyenda pamodzi ndi Mulungu ndiponso kuti akhale Mkhristu wamphamvu.

Mulungu anamvera mapemphero athu. Mayiyu anayamba kumabwera mokhulupirika ku tchalitchi. Nthaŵi iliyonse imene tinali kubwera kudzamuchezera kunyumba kwake, ayi ndithu, anali kumvetsetsa zedi Mawu a Mulungu. Iyeyu anaphunzira kupemphera ndi mphamvu kotero anayamba kuuza anthu ena zimene Mulungu anamuchitira.

Pamene tinali kupemphera, Mulungu analinso kukamba naye za moyo wake wakale. Mayi ameneyo nkuti ataba nkhuku zisanu ndi ziŵiri za mayi wina amene anayandikana naye nyumba. Mulungu anamusonyeza kuti iye ayenera kuti abweze nkhuku zisanu ndi ziŵiri zija anabazi kwa mwini wake, ndipo iye anabwezadi. Ndipo Mulungu anamukumbutsanso za zinthu zimene anaba ku sitolo, ndipo anapitanso kwa wogulitsa uja kukabvomereza machimo ake.

Tsiku lina nthenda yosadziŵika bwino inamugwira. Sitidziŵa chifukwa chake chenicheni nthenda imeneyi inabwera kwa iye. Mwina mwake tsiku lina tidzamvetsetsa. Mayi ameneyu sanalikutha kulankhula. Nthaŵi zina anali kungonena mawu pang'ono chabe. Nthaŵi zinanso sanali kulonjera anthu nkomwe. Nthenda imeneyi inapitiririrabe mpaka sabata ya thunthu.

Pa sabata anabwera ku tchalitchi, koma sanali kulankhula ndi anthu amene anamlandira. Msonkhano utatha, Akhristu asanu ndi atatu anamutengeranso m'tchalitchi kukampempherera. Ife tinatsimikiza kuti mzimu woipa ndiwo unali kumletsa kulankhula.

Timakumbukira kuti Yesu ananenapo za mizimu yoipa. Tinapemphera ndipo tinaulamula mzimu woipa uja kuti utulukemo mwa Mayi uja m'dzina la Yesu. Pambuyo pake tinamufunsa mayi uja kuti apemphere, koma sanathe konse. Tinayimba nyimbo za Yesu ndipo kenaka tinapemphera. Tinamufunsa kuti atchule dzina la Yesu. Koma sanathe konse. Tinapitirizabe kupemphera ndipo pomaliza iye anati, "Yesu," koma sananene kuti anali mwana wa Mulungu.

Tinapitirizabe kupemphera kokwanira ma ora aŵiri mpaka pomaliza chiŵanda chija chinamusiya. Kenaka anamwetula mlomo wake kwambiri nafuna kuseka. Iye anathokoza Mulungu m'dzina la Yesu mwana wa Mulungu. Iye anayimba ndi kupemphera. Anagwira manja athu ndipo anayamba kulankhula nafe popanda chobvuta chilichonse.

Tonse tinamtama Mulungu chifukwa choyankha pemphero lathu. Mwina mwake mumadziŵa wina wake amene akubvutika ndi ziŵanda za mtundu umenewu. Sichofuna cha Mulungu kuti iwo azibvutika m'njira imeneyi. Iyi ndi ntchito yathu ya ife Akhristu yopemphera m'dzina la Yesu kuti ziŵandazo zichoke. Lero lino mpempheni Mulungu kuti akusonyezeni wina wake amene alikubvutika m'njira yomweyi. Tayambani tsopano kumpempherera munthu ameneyu kuti apulumutsidwe.

Marko 9:29:

> Ndipo Iye anati kwa iwo; mtundu uwu sukhoza kutuluka ndi kanthu kena konse, koma ndi kupemphera.

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: MAYANKHO A MAPEMPHERO
TSIKU LACHISANU:

Pano palinso yankho lina la mapemphero limene linabwera kupyolera m'ntchito ya Moyo Watsopano Kwa Onse (New Life for All). Izi zinachitika ku Zambia.

Mmene chiphunzitso cha Moyo Watsopano Kwa Onse (New Life for All), chinayambika ku Zambia, anthu ambiri anayambitsa timagulu tating'ono-ting'ono tamapemphero. Ena mwa anthu ameneŵa anali kukumana m'maŵa. Ena madzulo.

Amayi ena ochokera m'boma la Solwezi m'dziko la Zambia anayambitsa gulu lopemphera. Iwo anaganiza kuti ayenera kugwirizana m'mapemphero kuti apulumutse sing'anga wa ufiti amene anali kugwira ntchito pafupi ndi iwo. Kunali kunenedwa kuti munthu ameneyu anali ndi misasa yambiri kudzanso omuthandiza ake atatu amene anali kudziŵa matenda ndi kupereka mankhwala ake. Amayiwo anali kumpempherera tsiku ndi tsiku mwa kutchula dzina lake, kuti Mulungu ampulumutse kuzochimwa zake, ndi kuzochita zake za usatanazo.

Patapita sabata zingapo, amayi aja anaganiza kuti akalankhule naye munthu uja kuti akhale Mkhristu. Koma iwo anali ndi mantha kuti amuuze, koma pomaliza anapita kukamuchezera. Iwo anamuuza mmene Mulungu angamupulumutsire kumachimo ake ndi kumpatsa moyo watsopano. Iye anafunsa mafunso ambiri. Mafunso ena sanali kutha kuŵayankha. Iwo anamuuza kuti anali asanazidziwe zinthu zimenezi, koma anali otsimikiza kuti iye anali kusoŵa moyo watsopano ndipo Mulungu akhoza kumupatsa. Pambuyo pake munthu uja anabvomereza zimene amayi aja ananena ndipo anapemphera pemphero kotero kuti anatembenuka mtima.

Pamene amayi anabwerera kumudzi ndi kukanena kuti sing'anga wa ufiti uja watembenuka mtima, anthu sanakhulupirire. Koma pambuyo pake a Samueli Kasonso, mkulu wa gulu la New Life for All, (Moyo Watsopano Kwa Onse) mu Zambia monse, anapita kukayendera dera limeneli. Ali chiyendetsere galimoto yawo, anaone munthu wina amene anaima pamsewu ndi mkazi wake kufuna chithandizo cha galimoto ndipo iwo anamtenga m'galimoto yawo. Pamene anayamba kuyenda, anayamba kulonjelana kuti adziŵane wina ndi mnzake. Ndipo Bambo Kasonso mwini galimoto

uja anafunso munthuyo kuti dzina lake ndani. Bambo uja pamene anaŵauza Bambo Kasonso dzina lake, anazindikira kuti iyeyu anali sing'anga wa ufiti uja. Iwo anamufunsa Bambo uja za ntchito yake ya using'anga momwe ili kuyendera. Bambo uja anayankha nati, "Kalero ndinali sing'anga, koma masiku ano ndine Mkhristu. Ndinalandira Khristu kukhala Mpulumutsi wanga ndipo masiku ano sindili kugwiranso ntchito ya mtundu umene uja, ayi."

Pambuyo pake a Kasonso anafunsitsa kwa anthu za sing'angayo. Ndipo anthu enawo anachitira umboni kuti, "Indedi zoona," analapadi ndipo sali kuchiritsanso anthu tsopano. Masiku ano amabwera ku tchalitchi.

Mwina mwake m'mudzi mwanu muli sing'anga monga ngati ameneyu. Mwina mwake kuoneka ngati mkovuta kumpempherera. Musachite mantha kumbukirani amayi akumpoto kwa Zambia aja amene analibe mantha pakupemphera. Taimani tsopano ndipo yambani kumpempherera sing'anga wa ufitiyu amene muli naye pafupi kuti adzapeze moyo watsopano mwa Khristu.

Mupemphererenso amene analapa ku Zambia uja. Iye ali kuyesedwa kuti abwererenso ku ntchito yake yakale. Mupempherereni kuti asadzaigwirenso ntchito yakeyo mpaka muyaya.

Machitidwe 19:18-19:

> Ndipo ambiri a iwo akukhulupirirawo anadza, nabvomereza, nafotokoza machitidwe awo, ndipo ambiri a iwo akuchita zamatsenga anasonkhanitsa mabuku awo, naŵatentha pamaso pa onse; ndipo anawerenga mtengo wake, napeza ndalama za siliva zikwi makumi asanu.

SABATA LAKHUMI: PEMPHERO LA AMBUYE NDI KUBWEREZA
TSIKU LOYAMBA:

Sabata yomalizayi tikufuna kuti tionenso mwamsanga zimene taphunzira m'maphunziro aŵa ndipo kuti tizisunge m'mitima mwathu. Tingathe kuchita zimenezi titayamba taona lemba lina m'Buku Lopatulika.

Taphunzira kale pa Mateyu 6 kuti Yesu anali kuphunzitsa ophunzira ake zakupemphera. Atatha kuŵauza zinthu zina zake za mapemphero, Iye anaŵapatsa chitsanzo chakupemphera. Pemphero limene anaŵapatsa, nthaŵi zonse limatchedwa Pemphero la Ambuye. Mmenemo timapezamo zinthu zambiri zimene taphunzira kale za mapemphero.

Mateyu 6:9-13:

> Chifukwa chake pempherani inu chomwechi;
> Atate wathu wa kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe. Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe, monga kumwamba chomwecho pansi pano. Mutipatse ife lero chakudya chathu cha lero. Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhululukira amangawa athu. Ndipo musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo. Chifukwa wanu uli ufumu, ndi mphamvu ndi ulemelero wa nthaŵi zonse. Amen.

1. Kodi mwaloweza pamtima pemphero la Ambuyeli? ________

==========================================================

Kupemphera pemphero ili monga mmene lililimu ndi njira yabwino kwambiri yopemphera, ngati muli kuganiza za mawu ndi kupemphera ndi mtima wanu wonse. Koma nthaŵi zina anthu amangolibwereza-bwereza mosaganizira. Ndipo iwo amati apemphera. Koma sizimene anatanthauza Yesu. Uku sikupemphera ayi.

2. Ngati tifuna kupemphera pemphero la Ambuye, kodi tiyenera kupemphera bwanji?

________________________________